## PHUNZIRO LA 28

1.Kodi chifukwa chiyani chitsamba chimene chim-kayakacho sichimkapsa?
-Chifukwa chakuti Mulungu anali mchitsambacho.

2. Kodi amene anali ngati chitsamba chimene chinkayaka koma osapserera anali ndani?
-A Isirayeli.

3. Kodi a Isirayeli ali bwanji ngati chitsamba chimene chinkayakacho?
-Satana ndi Farawo ankafuna kuŵawononga a Isirayeli ngati m'mene moto unkafunira kuwononga chitsamba chimene chinkayakacho.
-Mulungu anali ndi a Isirayeli ngati m'mene analili mchit-samba chimene chinkayakacho.

4. Kodi dzina lakuti "NDILIPO" limatanthawuza chiyani?
-Limatanthandawuza kuti Mulungu alibe chiyambi.
-Limathandawuza kuti Mulungu alibe mathelo.
-Limatanthawuza kuti Mulungu wakhala alipo nthaŵI zonse.
-Limatanthawuza kuti palibe nthaŵI imene Mulungu kunalibe.

5. Kodi Mulungu anadziŵa kuti Farawo sakaŵalora a Isirayeli kuchoka mu Ejipito?
-Inde.
-Mulungu amadziŵa china chilichonse.

6. Kodi chizindikiro choyamba chowonetsa kuti Mulungu anamusankha Mose kuti akaŵatsogolele a Isireyeli kutuluka mu Ejipito chinali chotani?
-Ndodo ya Mose inasanduka njoka, kenako inabweleranso kukhala ndodo.

7. Kodi chizindikiro chachiŵiri chowonetsa kuti Mulungu anamusankha Mose kuti akaŵatsogolele a Isireyeli kutuluka mu Ejipito chinali chotani?
-Dzanja la Mose linasanduka kukhala la khate iye atalilowetsa m'mchovala mwake, ndipo linasandukanso kukhala labwinobwino atalilowetsanso mchovala chakecho.

8. Kodi Mulungu anamutumiza ndani kuti akamuthandize Mose kulankhula kwa Farawo?
-Mbale wake wa Mose, Aroni.

9. Kodi chifukwa chiyani Mulungu ankafuna kuti aŵapulumutse a Isirayeli mu ukapolo.
-Chifukwa chakuti Mulungu anaŵakonda a Isirayeli, ndipo Iye sanafune kuti iwowo akhale mu ukapolo.
-Chifukwa chakuti Mulungu anamulonjeza Aburahamu kuti adzaŵatsogolera iwowo kubwelera ku dziko la Kanani.
-Chifukwa chakuti Mulungu anamulonjeza Aburahamu kuti adzatumiza Mpulumutsi kupitira mwa a Isirayeli.

-Mulungu anasunga lonjezo lake kwa Mose, ndipo anamutumiza Aroni, m'bale wake wa Mose kuti akamuthandize Mose.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 4:27-28

27-AMBUYE analankhula ndi Aroni kuti, "Pita ku chipululu kuti akawonane ndi Mose." Chomcho iye anapita ndipo anakakumana ndi Mose ku phiri la Mulungu, ndipo anamumpsompsona.
28-Mose anamuwuza Aroni mawu onse amene AMBUYE anamuwuza, pa nthaŵI imene ankamutumayo. Anamuwuzanso za zizindikiro zozizwitsa zonse zimene anamulamula kuti akazichite.



-Kodi chifukwa chiyani milili yonseyi siyimafika ku malo amene a Isirayeli amakhala?

-Chifukwa chakuti Mulungu anamulonjeza Aburahamu, Isaki ndi Yakobo kuti adzaŵadalitsa, ndipo adzaŵasandutsa kukhala mtundu wotchuka ndipo wawukulu.

-Chifukwa chakuti Mulungu ankamuwonetsa Farawo, a Ejipito pamodzi ndi a Isirayeli, kuti Iye yekha ndiye Mulungu, ndipo palibenso wina.

-Ngakhale kuti Mulungu anatumiza milili yowopsa ngati imeneyi, Farawo anakanabe kuŵalola a Isirayeli kupita.

-Ngakhale kuti Mulungu anatumiza milili yowopsa ngati imeneyi, Farawo anakanabe kumumvera Mulungu.

-Kodi Farawo angalimbane ndi Mulungu ndikupambana?
-Iyayi.

-Kodi pali amene angalimbane ndi Mulungu ndikupambana?
-Palibe.

-Kodi chidzaŵachitikire ndi chiyani anthu amene amamenyana ndi Mulungu?
-Mulungu adzaŵawononga iwowo.

m'mitengo zimene matalala adasiyako. Palibe chachiŵisi chilichonse chimene chidatsalako pa mtengo kapena pa chomera china chilichonse m'dziko lonse la Ejipito.

-Farawo anamupempha Mose kuti awuchotse muliliwo, ndipo aŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Koma Mulungu atachotsa mulili umenewo, Farawo anakana kuŵalola a Isirayeli kupita.

-Mulili wachisano ndi chinayi, Mulungu anatumiza mdima kwa masiku atatu umene anadzadza pa dziko lonse la Farawo pamodzi ndi a Ejipito.

-Koma mulili umenewu, siwunafike ku malo kumene amakhala a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 10:21-23

21-Pambuyo pake AMBUYE anamuwuza Mose kuti, "Kweza dzanja lako kumwamba kuti pagwe mdima wandiwe yani pa dziko lonse la Ejipito."
22-Mose adakweza dzanja lake kumwamba, ndipo pa masiku atatu mudagwa mdima wandiwe yani m'dziko lonse.
23-A Ejipitowo sankathanso kuwonana, ndipo palibe ndi m'modzi yemwe amene adachoka pa khomo pake masiku atatu onsewo. Koma a Isirayeli okha ankakhala kowala ndithu kuja ankakhalaku.

-Farawo anamupempha Mose kuti awuchotse muliliwo, ndipo aŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Koma Mulungu atachotsa mulili umenewo, Farawo anakana kuŵalola a Isirayeli kupita.



-Kenako Mose ndi Aroni anapita ku Ejipito.

-Mose ndi Aroni atafika ku Ejipito, anaŵasonkhanitsa a Isirayeli onse pamodzi, ndipo anaŵawuza zonse zimene Mulungu anamuwuza mose.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 4:29-31

29-Mose ndi Aroni anapita ku Ejipito ndipo anakaŵasonkhanitsa akuluakulu onse a a Isirayeli.
30-Aroni anaŵawuza akuluakulu aja zonse zimene AMBUYE anamuwuza Mose ndipo anachita zizindikiro zozizwitsa zija, anthuwo akuwona.
31-Anthuwo anamukhulupilira. Ndipo atamva kuti AMBUYE adadzaŵayendera a Isirayeli, ndipo kuti adakuwona kuvutika kwawo, anaŵeramira mitu yawo pansi napembedza.

-Kodi a Isirayeli anaŵakhulupilira mawu a Mulungu amene IYE anamuwuza Mose?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani kunali kwabwino kwa a Isirayeli kumvera mawu a Mulungu?

-Chifukwa chakuti Mulungu yekha ndi amene anakatha kuŵapulumutsa a Isirayeli.
-Chifukwa chakuti mawu a Mulungu okha ndi amene anakatha kuŵapulumutsa a Isirayeli.

-Ngati ife sitikuŵakhulupilira mawu a Mulungu, ndiye kuti ife tikumutcha Mulungu kuti ndiwabodza.

-Kodi Mulungu adzaŵapulumutsa anthu amene sakuŵakhulupilira mawu a Mulungu?

-Iyayi.

-Ngati sitikuŵakhulupilira mawu a Mulungu, ndiye kuti sitingapulumutsidwe.

-Mulungu amafuna kuti inu mudzimvera mawu a Mulungu kuti mukapulumutsidwe.

-Mulungu yekha ndi amene angaŵapulumutse anthu.
-Mawu a Mulungu okha ndi amene angaŵapulumutse anthu.

-Mose ndi Aroni atatha kulankhulana ndi anthu, anapita kukalankulana ndi Farawo.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 5:1-2

1-Pambuyo pake, Mose ndi Aroni anapita kwa Farawo nakamuwuza kuti, "Naŵa mawu a AMBUYE, Mulungu wa a Isireyeli, akunena kuti, " "Uŵalole anthu anga apite ku chipululu kuti akachite mwambo wa chipembedzo wondilemekeza Ine."
2-Farawo adayankha kuti, "Kodi AMBUYEWO ndi ndani kuti ine nkumvera zimenezo ndikuŵalora a Isirayeli kuti apite? AMBUYEWO sindikuŵadziŵa, ndipo sindidzalora konse kuti a Isirayeli apite."

-Kodi Farawo anayankha kuti chiyani pamene Mose anamuwuza iye kuti Mulungu akumulamula iye kuti aŵalole a Isirayeli kuti adzipita?

-Farawo anati, "Sindikuŵadziŵa AMBUYE, ndipo sindiŵalola a Isirayeli kuti adzipita."

-Kodi chifukwa chiyani Farawo sankamudziŵa Mulungu?



wepo.
25-Matalalawo adawononga zonse zokhala panja m'dziko lonse la Ejipito, anthu onse pamodzi ndi nyama zomwe. Adawononganso zomera zonse za m'minda ndikukadzulanso mitengo yonse .
26-Dziko la Goseni lokha, kumene kunkakhala a Isirayeli, matalalawo sadagweko mpang'ono pomwe.

-Farawo anamupempha Mose kuti awuchotse muliliwo, ndipo aŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Koma Mulungu atachotsa mulili umenewo, Farawo anakana kuŵalola a Isirayeli kupita.

-Mulili wachisano ndi chitatu, Mulungu anatumiza dzombe, ndipo linadya mitengo ndi zomera zonse za Farawo pamodzi ndi a Ejipito zimene zinatsala ku mulili wa matalala, mphenzi ndi mabingu uja.

-Koma mulili umenewu, siwunafike ku malo kumene amakhala a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 10:13-15

13-Chomcho Mose adakweza ndodo yake kumwamba, ndipo AMBUYE adawutsa mphepo ya ku vuma kuti iwombe pa dziko usana ndi usiku omwe.
Pamene kunkacha, nkuti ponseponse pali dzombe lokhalokha.
14-Lidangophimba dziko lonse, ndipo lidakhazikika m'dzikomo. Kuchuluka kwake kwa dzombelo kunali kwakuti nkale lonse dzombe lotero silidawonekepo, ndipo silidzawonekanso.
15-Lidangophimba nthaka yonse, ndipo nthakayo inada kuti bii chifukwa cha dzombelo. Dzombelo lidadya kena kalikonse komera pa nthaka, pamodzi ndi zipatso za

-Koma mulili umenewu, siwunafike ku malo kumene ama-
khala a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 9:10

10-Chomcho Mose adatapa phulusalo pa moto ndipo adakayimilira pa maso pa Farawo. Adawaza phulusalo kumwamba, ndipo padabuka zithupsa zimene zidaphulika ndikusanduka zilonda pa anthu ndi pa nyama zomwe.

-Farawo anamupempha Mose kuti awuchotse muliliwo, ndipo aŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Koma Mulungu atachotsa mulili umenewo, Farawo anakana kuŵalola a Isirayeli kupita.

-Mulili wa chisano ndi chiŵiri, Mulungu anatumiza mabingu, mphenzi ndi matalala, zinali pa dziko lonse la Ejipito, ndipo zinawononga mitengo yonse pamodzi ndi mbewu zonse za Farawo ndi a Ejipito.

-Koma mulili umenewu, siwunafike ku malo kumene amakhala a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 9:23-26

23-Mose adakweza ndodo yake kumwamba. Pompo AMBUYE anatumiza mabingu ndi matalala, ndipo mphezi zidawomba pa nthaka.
AMBUYE adagwetsa matalala pa dziko lonse la Ejipito.
24-Ndipo panali mvura ya matalala ndi mphezi zong'anima kwambiri. Matalala ake anali owopsa kwambiri, kotero kuti chiyambire pamene a Ejipito anasanduka mtundu wa anthu oyima pawokha, matalala otere sadag-



-Chifukwa chakuti Farawo sankafuna kuti amudziŵe Mulungu.
-Chifukwa chakuti Farawo sankafuna kuti akhulupilire mwa Mulungu.
-Chifukwa chakuti Farawo ankaŵakonda machimo ake.

-Farawo ndi anthu a ku Ejipito sankakhulupilira mwa Mulungu.

-Farawo ndi anthu a ku Ejipito ankapembedza mtsinje wawukulu umene unali m'dziko mwawo.
-Farawo ndi anthu a ku Ejipito ankapembedza dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi.

-Farawo ndi anthu a ku Ejipito ankapembedza nyama zambiri.
-Anthu a ku Ejipito ankamupembedzanso Farawo ngati mulungu wawo.

-Farawo  ndi anthu a ku Ejipito ankazipembedza zinthu zimene Mulungu anazilenga m'malo mumupembedza Mulunguyo.

-Mu nthaŵI ya Farawo, anthu ambiri ankakana kukhulupilira zowona zenizeni za Mulungu.

-Masiku ano, anthu ambiri amakananso kukhulupilira zowona zenizeni za Mulungu.

-Chifukwa chakuti anthu ambiri amakana kukhulupilira zowona zenizeni za Mulungu, Mulungu anamulola Satana kuti adziŵanamiza iwowo.

-Satana anaŵanamiza anthu, ndipo anthuwo amazipembedza zinthu zimene Mulungu anazilenga.
-Chifukwa chakuti anthu ambiri anakana kukhulupilira

zowona zenizeni za Mulungu, Mulungu anamusankha Aburahamu kuti akhale kholo la a Isirayeli.

-Mulungu anasankha zotumiza Mpulumutsi kupitira mwa Aburahamu ndi a Isirayeli.

-Mulungu anasankhanso zolemba zowona Zake zenizeni M'buku Lake, limene analilemba kupitira mwa Aburahamu ndi a Isirayeli.

-Buku la Mulungu limatchedwa kuti Bayibulo.

-Kodi Mulungu anadziŵa kuti Farawo sakaŵalola a Isireyeli kutuluka m'dziko lake la Ejipito?
-Inde.

-Mulungu amadziŵa china chilichonse ngakhale chisanachitike.

-Farawo atakana kuŵalola a Isirayeli kupita, imvani zimene Mulungu analankhula kwa Mose:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 6:1

1-AMBUYE adamuwuza Moseyo kuti, "Uwona tsopano zimene ndimuchite Farawo. Ndidzamukakamiza Farawo kuti aŵatulutse anthu anga m'dziko lake. Ndithudi adzaŵatulutsiratu m'dzikomo, chifukwa chakuti ndidzamukakamiza ndi dzanja langa la mphamvu. Zowonadi, dzanja langa la mphamvu lidzamuwumilira kuti aŵapilikitse."

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaganiza zowonetsa mphamvu zake zambiri kwa Farawo pamodzi ndi a Isirayeli?
-Kuti adziŵe kuti Iye yekha, ndiye Mulungu weniweni.



ba za nduna zake, ndiponso dziko lonse la Ejipito. Dziko lonselo lidayipiratu ndi mizazayo.

-Farawo anamupempha Mose kuti awuchotse muliliwo, ndipo aŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Koma Mulungu atachotsa mulili umenewo, Farawo anakana kuŵalola a Isirayeli kupita.

-Mulili wachisano, Mulungu anatumiza imfa za nyama, ndipo mahachi, ng'ombe, nkhosa, ngamila ndi abulu onse a Farawo pamodzi ndi a Ejipito, anafa.

-Koma mulili umenewu, siwunafike ku malo kumene amakhala a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 9:6-7

6-Tsopano AMBUYE adachitadi monga m'mene ananenera, ndipo ziweto zonse za a Ejipito zidafa. Koma padalibe chiweto m'chimodzi chomwe cha a Isireyeli chimene chidafapo.
7-Ndipo Farawo atafunsitsa zimene zinachitikazo, adamva kuti palibe chiweto mchimodzi chomwe cha a Isirayeli chimene chidafapo. Komabe Farawo adakhala okanika ndithu, ndipo sadalole konse kuti anthuwo apite.

-Farawo anamupempha Mose kuti awuchotse muliliwo, ndipo aŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Koma Mulungu atachotsa mulili umenewo, Farawo anakana kuŵalola a Isirayeli kupita.

-Mulili wachisano ndi chimodzi, Mulungu anatumiza zithupsa, ndipo Farawo pamodzi ndi a Ejipito onse anadzadzidwa ndi zithupsa m'matupi mwawo.

wo pamodzi ndi a Ejipito, ndi dziko lonse la Ejipito, linad-
zadzidwa ndi nthata.

-Koma mulili umenewu, siwunafike ku malo kumene ama-
khala a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 8:16-17

16-Pamenepo AMBUYE anamulamula Mose kuti, "Umuwuze Aroni kuti asamule ndodo yake ndipo amenye pa nthaka, chomcho fumbi lonse m'dziko lonse la Ejipito lidzasanduka nthata.
17-Iwowo adachitadi momwemo. Aroni adasamula ndodo yale ija namenya pa nthaka. Ndipo fumbi lonse lida-sanduka nthata, ndipo zidabalarikira pa anthu ndi nyama zomwe. Motero fumbi lonse la mu Ejipito lidangokhala nthata zokhazokha.

-Farawo anamupempha Mose kuti awuchotse mulilìwo, ndipo aŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Koma Mulungu atachotsa mulili umenewo, Farawo ana-kana kuŵalola a Isirayeli kupita.

-Mulili wachinayi, Mulungu anatumiza mizaza, ndipo Fara-wo pamodzi ndi a Ejipito, ndi dziko lonse la Ejipito, linad-zadzidwa ndi mizaza.

-Koma mulili umenewu, siwunafike ku malo kumene ama-khala a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 8:24

24-Chomcho AMBUYE adachitadi zimenezi, ndipo magulu a mizaza adaloŵa mnyumba ya Farawo, mnyum-



-Mulungu anaganiza zomuwonetsa Farawo ndi a Ejipito kuti mtsinje wawukulu umene unali m'dziko mwawo, siwunali Mulungu.

-Mulungu anaganiza zomuwonetsa Farawo ndi a Ejipito kuti dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi sizinali Mulungu.

-Mulungu anaganiza zomuwonetsa Farawo ndi a Ejipito kuti nyama zawo zambirizo, sizinali Mulungu.

-Mulungu anaganiza zomuwonetsa Farawo ndi a Ejipito kuti Farawoyo sanali Mulungu.

-Mulungu anaganizanso zowonetsa mphamvu zake kwa a Isirayeli kuti iwo adziŵe kuti Iye anali Mulungu wawo.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 6:2-8

2-Mulungu analankhula ndi Mose namuwuza kuti, "Ine ndine AMBUYE.
3. Ndinawonekera kwa Aburahamu, Isaki ndi Yako-bo ngati Mphambe, koma sindinaŵadziŵitse dzina langa kuti ndine AMBUYE.
4-Ndanachita nawo chipangano ndikuŵalonjeza kuti ndidzaŵapatsa dziko la Kanani, momwe adakhala kale ngati alendo.
5-Tsopano ndamva kudandawula kwa a Isirayeli, amene ali mu ukapolo wa a Ejipito, ndipo ndakumbukira chipangano changa.
6-Tsopano iwe ukaŵawuze a Isirayeli mawu anaga akuti, "Ine Ndine AMBUYE. Ndidzakutulutsani mu ukapolo wa ntchito yakalavula gaga imene a Ejipito akukukakami-zani kuyigwira. Ndidzakupulumutsani ndi dzanja langa lo-tambalala ndipo pochita ntchito zamphamvu.
7-Inu mudzakhala anthu anga, Ine ndidzakhala

Mulungu wanu Mudzazindikira kuti ndine AMBUYE, Mulungu wanu, amene ndinakupulumutsani ku ntchito yakalavula gaga yimene a Ejipito akukukakamizani kuyigwira.

8-Ndipo ndidzakufikitsani ku dziko limene ndinalumbira kuti ndidzalipereka kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo. Ndidzakupatsani dziko limenelo kuti likhale lanulanu. Ine ndine AMBUYE."

-Mulungu anaganiza zowonetsa nphamvu zake kwa a Isirayeli kuti iwo adziŵe kuti Iye anali Mulungu wa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo.

-Mulungu anaganiza zowonetsa nphamvu zake kwa a Isirayeli kuti iwo adziŵe kuti Iye anali Mulungu wawo, Mulungu wa a Isirayeli.

-Chifukwa chakuti Farawo sanaŵalole a Isirayeli kuchoka m'dziko lake, Mulungu anayamba kuwonetsa mphamvu Zake zambiri.

-Kodi Mulungu anawonetsa bwanji mphamvu Zake zambirizo kwa a Ejipito ndi a Isirayeliwo?

-Mulungu anatumiza milili yambiri kwa Farawo ndi a Ejipito

-Mulili woyamba, Mulungu anaŵasandutsa madzi a mu mtsinje wawukulu wa m'dziko la Ejipito kukhala magazi.

-Koma mulili umenewu, siwunafike ku malo kumene amakhala a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 7:20-21

20-Chomcho Mose ndi Aroni anachita monga m'mene AMBUYE anaŵalamulira. Aroni adasamula ndodo



yake namenya madzi a mu mtsinje pa maso pa Farawo ndi nduna zake, ndipo madzi onsewo adasanduka magazi.

21-Msomba zonse za mu mtsinje wa Nayilo zidafa, ndipo kununkha kwake kwa madziwo kunali kwakuti a Ejipito sanathenso kuŵamwa. Ndipo munali magazi okhaokha m'dziko lonse la Ejipito.

-Farawo anamupempha Mose kuti awuchotse muliliwo, ndipo aŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Koma Mulungu atachotsa mulili umenewo, Farawo anakana kuŵalola a Isirayeli kupita.

-Mulili wachiŵiri, Mulungu anatumiza achule, ndipo dziko lonse la Farawo pamodzi ndi anthu ake anadzadzidwa ndi achule.

-Koma mulili umenewu, siwunafike ku malo kumene amakhala a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 8:5-6

5-AMBUYE anamuwuzanso Mose kuti, "Umuwuze Aroni kuti, "Uloze ndodo yake ku mitsinje, ku ngalande ndi ku zithaphwi ndipo pakhale achule pa dziko lonse la Ejipito."

6-Chomcho Aroni adaloza ndodo yake pa madzi, ndipo achule adatuluka , nadzadza pa dziko lonselo.

-Farawo anamupempha Mose kuti awuchotse muliliwo, ndipo aŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Koma Mulungu atachotsa mulili umenewo, Farawo anakana kuŵalola a Isirayeli kupita.

-Mulili wachitatu, Mulungu anatumiza nthata, ndipo Fara-